## UNDUNA WA ZACHILENGEDWE NDI KUSINTHA KWA NYENGO

NTHAMBI YOWONA ZANYENGO NDI KUSINTHA KWA NYENGO

# NYENGO MSABATAYI


## KUYAMBIRA PA 30 SEPTEMBER MPAKA 6 OCTOBER, 2024

### NYENGO M'SABATA IKUBWERAYI

Tiyembekezere **nyengo ya dzuwa,** ya changululu **ndi yotentha kwambiri** kupitirira mpaka masana a Lachiwiri pa 1 October, 2024. Koma, kuyambira usiku wa Lachiwiri pa 1 October mpaka Lamulungu pa 6 October 2024, **kudzakhala kwa mitambo, kwa mphepo ndipo madigiri akatenthedwe adzatsika, komanso kudzagwa mvula m'madera ochuluka yomwe idzagwa mwa mphamvu ndi ya mabingu m'madera ena. Mphepo ya Mwera idzawombanso pa nyanja ya Malawi ndi nyanja zina** kuyambira usiku wa Lachiwiri pa 1 October.

### NYENGO MU SABATA YANGOTHAYI

M'madera ambiri kunatentha kuposa mlingo okhazikika wa mwezi wa September. Ku Monkey Bay ndi komwe kunatentha kwambiri poyerekeza ndi mlingo okhazikika ndi madigiri oposera **+10.0°C**, ndipo madigiri anafika **39.6°C**. Aka ndi koyamba madigiri kufika mlingo umenewu mu m'mwezi wa September ku Monkey Bay. Pa 27 September, ku Chikwawa kwa Ngabu kunatentha kwambiri ndi madigiri **40°C** (Zambiri onani mapu ali m'musiwa). Lolemba, m'madera ena am'zigawo za kum'mwera ndi kumpoto kunagwa mvula yomwe inagwa ya mulingo wa 17.2 mm ku Mulanje ndipo inafika 12.5 mm ku Mzuzu.




*Mapu: Mlingo wa katenthedwe pofananiza ndi mlingo wokhazikika wa 1991 mpaka 2020*

### MALANGIZO M'SABATALI

- **Pa nyanja:** Tikhale osamala nthawi yomwe kukuomba mphepo ya Mwera.
- **Nyengo yotentha ndi ya dzuwa:** Tizimwa madzi pafupipafupi komanso tisamakhalitse pa dzuwa.
- **Mvula ya mabingu:** Tibisale malo otetezeka bwino kukamaomba mphenzi, tionetsetse kuti nyumba zathu sizingasasuke mosavuta ndi mphepo ya mkuntho.

***Kuti mudziwe zambiri funsani kwa:*** *The Director, Department of Climate Change and Meteorological Services, Ministry of Natural Resources and Climate Change, P. O. Box 1808, Blantyre, Malawi. Tel: (265) 882 266 579; Email: metdept@metmalawi.gov.mw , Website: www.metmalawi.gov.mw*

**Malo osindikizira: Blantyre** **Yatulutsidwa Lamulungu pa 29 September, 2024**